26 جمادى الأولى 1446
28/11/2024

# الإسلام دين الفطرة والعقل والسعادة

# CHISILAMU

# CHISILAMU

## Chipembedzo chogwirizana ndi chilengedwe, nzeru ndi chobweresa chisangalalo.

M'dzina la Mulungu ,Wachifundo Chambiri ,Wachisoni Chosatha.

Kodi unayamba wazifunsa wekha?

Kodi ndi ndani amene adalenga mitambo ndi nthaka,komanso zolengedwa zazikulu zikupezeka ku mitambo ndi pansi pa nthaka? Kodi ndani adapanga ndondomeko yokuya ndi yokonzedwa mwa ukadaulo?

Kodi dziko lalikululi zimatheka bwanji zinthu kuchitika mwa ndondomeko komanso mokhazikika potengera malamulo okuya omwe akhala akulitetedza dzikoli kwa zaka zochuluka?

Kodi Dzikoli lidazilenga lokha? Kapena zinachokera pachabe? Kapena zinangopezeka mwangozi?

### Ndani adakulenga iwe?

Kodi ndi ndani amene adaika ndondomeko yodzama mu ziwalo za pa thupi pako komanso ziwalo za zinyama za moyo?

Palibe amene angavomereze kuuzidwa kuti nyumbayi idabwera popanda wina kumanga! Kapena kumuuza kuti nyumbayi ilibe yemwe anaibweretsa! Kodi anthu ena angakhulupirire bwanji anthu amene amanena kuti chilengedwe chonsechi chinabwera popanda Mlengi? Kodi munthu woganiza bwino angavomereze bwanji kuuzidwa kuti dongosolo lolondola lachilengedwechi linangopezeka mwangozi?

Ndithu, kuli Mulungu wamkulu, Mlengi ndi Wolamulira wa chilengedwe chonse ndi zonse zili m’menemo, ndipo Iye ndi Mulungu Wamphamvu zonse.

Ndipo Ambuye, Ulemelero ukhale kwa Iye, adatitumizira ife atumiki, ndipo adawatsitsira atumikiwo mabuku (chivumbulutso),ndipo lotsiriza mwa mabukuwo ndi buku la Qur’an lolemekezeka, limene Mulungu adalivumbulutsa kwa Muhammad, womaliza mwa atumiki a Mulungu, ndipo kudzera mwa mabuku ake ndi atumiki ake:

•Anatizindikiritsa ife za iye mwini, mbiri zake, ndi zoyenera kuti tizimuchitira, ndipo wafotokoza zoyenera iye kutichitira ife ngati tachita zoyenera kumuchitira iyeyo.

•Watisonyeza potidziwitsa kuti iye ndi Mbuye amene adalenga zolengedwa zonse, ndikuti iye ndi wa moyo mpaka kale sadzamwalira, ndipo zolengedwa zonse zili m'manja mwake,pansi pa mphamvu ndi ulamuliro wake.

Ndipo adatiuza kuti zina mwa mbiri zake ndi kudziwa, ndithu iye ngodziwa chilichonse, ndi kuti ngwakumva,kupeya ,ndipo palibe chobisika kwa iye padziko lapansi kapena kumwamba.

Ndipo Mbuye ndi wamoyo wamuyaya, okhazikika, amene mwa Iye yekha ndi m'mene moyo wa cholengedwa chilichonse umachokera, Ulemelero ukhale kwa Iye, ndipo ndi yemwe mwa iye wakhazikika moyo wa zolengedwa zonse, Ulemelero ukhale kwa iye wamphamvu zonse adati:

(اللَّهُ لا إِلَهَ إِلَّا هُوَ الْحَيُّ الْقَيُّومُ لا تَأْخُذُهُ سِنَةٌ وَلا نَوْمٌ لَهُ مَا فِي السَّمَوَاتِ وَمَا فِي الأَرْضِ مَنْ ذَا الَّذِي يَشْفَعُ عِنْدَهُ إِلَّا بِإِذْنِهِ يَعْلَمُ مَا بَيْنَ أَيْدِيهِمْ وَمَا خَلْفَهُمْ وَلا يُحِيطُونَ بِشَيْءٍ مِنْ عِلْمِهِ إِلَّا بِمَا شَاءَ وَسِعَ كُرْسِيُّهُ السَّمَوَاتِ وَالأَرْضَ وَلا يَئُودُهُ حِفْظُهُمَا وَهُوَ الْعَلِيُّ الْعَظِيمُ)

(Palibe Mulungu opembedzedwa mwa choonadi koma iye, wamoyo wamuyaya,odaliridwa ndi zolengedwa zonse,samasinza kapena kumupeza tulo,zolengedwa zonse zili ku mwamba ndi dziko lapansi zili m'manja mwake,palibe amene angakhale ndi mphamvu zomuthandiza wina pamaso pa Mulungu kupatula Mulungu ataloleza kuti zitero,amadziwa za zolengedwa zonse zomwe zinalipo kalekale,zomwe zili pano ndi zomwe zidzalengedwe msogolo,amadziwa za msogolo zomwe zidzachitikire zolengedwa zake komanso zomwe zinachitika kale,palibe cholengedwa chimadziwa zobisika zake kupatula zomwe iye Mulungu wachidziwitsa cholengedwacho,mpando wa ufumu wake malo ake ndi akulu monga m'mene kulili kumwamba ndi dziko lapansi,ndipo sizimamulemera kuzisunga ndikuteteza kumwamba ndi dziko lapansi,iye Mulungu ndi wapamwamba komanso wamkulu). [Suratu Al-Baqara:255]

•Ndipo adatiuza kuti Iye ndi Ambuye, amene amadziwika ndi mbiri zangwiro, ndipo adatipatsa maganizo ndi mphamvu zomwe zimazindikira zodabwitsa za chilengedwe Chake ndi mphamvu zake, zomwe zimatisonyeza ukulu wake, mphamvu zake, ndi ungwiro wa mbiri zake. ndipo anaika mwa ife chibadwa chimene chimasonyeza ungwiro Wake ndi kuti Iye sangadziŵike ndi kupunguka.

•Ndipo anatiphunzitsa kuti Ambuye ali pamwamba pa mitambo yake, ndipo salowa m'dziko lapansi, ndipo dziko lapansi silikhala mwa Iye.

•Ndipo anatiuza kuti tiyenera kugonjera kwa Iye, Ulemerero ukhale kwa Iye, pakuti Iye ndiye Mlengi wathu ndi Mlengi wa dziko komanso muyendetsi wake

Mlengi ali ndi mbili za ukulu ndipo sangadziŵike konse ndi kusoŵa kapena kupereŵera, Mbuye saiwala, samagona, sadya chakudya, ndipo sangakhale ndi mkazi kapena mwana. Zolemba zonse zomwe zili ndi chilichonse chotsutsana ndi ukulu wa Mlengi, sizili mbali ya chivumbulutso cholondola chomwe chidadza ndi Atumiki a Mulungu, mtendere ukhale pa iwo.

Mulungu adanena mu buku la Quran kuti:

(قُلۡ هُوَ ٱللَّهُ أَحَدٌ * ٱللَّهُ ٱلصَّمَدُ * لَمۡ يَلِدۡ وَلَمۡ يُولَدۡ * وَلَمۡ يَكُن لَّهُۥ كُفُوًا أَحَدُۢ)

(Nena -iwe Mtumiki -SAW- kwa amene akukufunsa mwachipongwe, mbiri za Mulungu wako-kuti Iye ndi Mulungu m'modzi, (alibe nzake),

Mulungu ndi wokhala ndi zonse wodaliridwa ndi zolengedwa zake.

sadabale (mwana) ndiponso sadaberekedwe.

ndiponso palibe aliyense wofanana ndi iye. [Al-Ikhlas:1-4].

Ngati mumakhulupirira kuti kuli Mulungu Mlengi...kodi munayamba mwadzifunsapo kuti cholinga cha chilengedwe chanu chinali chiyani? Kodi Mulungu amafuna chiyani kwa ife, ndipo cholinga cha kupezeka kwathu n'chiyani?

### Kodi n’kutheka kuti Mulungu anatilenga n’kutisiya osasamala? Kodi zingakhale kuti Mulungu analenga zolengedwa zonsezi popanda chifukwa kapena cholinga?

Zoona zake n’zakuti, Mbuye, Mlengi Wamkulu, “Mulungu,” anatiuza za cholinga chake pakulengedwa kwa ife, chomwe ndi kupembedza Mulungu yekha, ndi zimene amafuna kwa ife! ndipo Adatiuza kuti Iye yekha ndiye woyenera kupembedzedwa, ndipo adatifotokozera kudzera mwa atumiki ake, mtendere ukhale pa iwo, momwe tingamupembedzere? Kodi tingaziyandikitse bwanji kwa Iye potsatira malamulo Ake ndi kusiya zoletsa zake? Kodi tingapeze bwanji chiyanjano Chake? Timachenjeza za chilango chake, ndikutiuza za tsogolo lathu pambuyo pa imfa?

Ndipo Adatiuza kuti moyo wapadziko lapansi ndi mayeso chabe, ndi kuti moyo weniweni ndi wokwanira udzakhala m’moyo wapambuyo pa imfa.

Adatiuzanso kuti yemwe adzapembedza Mulungu monga momwe adamulamulira, nasiya zomwe adamuletsa. Adzakhala ndi moyo wabwino padziko lapansi ndi chisangalalo chamuyaya tsiku lomaliza, ndipo amene samumvera ndi kukanira iye adzapeza masautso padziko lapansi ndi chilango chamuyaya tsiku lomaliza.

### Chifukwa tikudziwa kuti sitingadutse moyo uno popanda aliyense mwaife kulandira mphotho ya zomwe adachita, zabwino kapena zoyipa; ndiye sipadzakhala chilango kwa ochita zoipa, komanso malipiro abwino kwa ochita zabwino?

Ndipo ndithu Mbuye wathu watiuza kuti munthu akakhale opambana tsiku lotsiriza popeza chisangalalo cha Mulungu, ndi kupulumuka ku chilango chake sizingatheke popanda kulowa chisilamu,komwe ndi kugonjera mwa Iye Mulungu ,kumupembedza iye yekha popanda omuphatikiza naye, kugonjera Iye pomvera, ndi kutsatira malamulo ake mwa nsangala ndikuvomera, ndiye watiuzanso kuti pa tsiku la chiweruzo iye sadzalandira chipmbedzo china kuchokera kwa anthu chosakhala chisilamu, Mulungu adanena kuti:

(وَمَن يَبۡتَغِ غَيۡرَ ٱلۡإِسۡلَٰمِ دِينٗا فَلَن يُقۡبَلَ مِنۡهُ وَهُوَ فِي ٱلۡأٓخِرَةِ مِنَ ٱلۡخَٰسِرِينَ)

(Ndipo amene angatsate Chipembedzo china chosakhala Chisilamu, sichidzalandiridwa kwa iye, ndipo iye tsiku lomaliza adzakhala mmodzi mwa anthu otaika [Al-Imran: 85].

Amene ayang'ana zimene anthu ambiri akupembedza lero; ampeza wina akupembedza munthu, wina akupembedza fano, wina akupembedza Nyenyezi, ndi zina zotero.Ndipo sizoyenera kwa munthu wanzeru kupembedza zina koma Mbuye wa zolengedwa zonse, wokwanira mu mbiri zake, nanga apembedza bwanji cholengedwa ngati iye mwini kapena chapansi kuposa iye! Mulungu wopembedzedwa sangakhale munthu, fano, mtengo, kapena nyama!

Zipembedzo zonse zomwe anthu akuzipembedza lero - kupatula Chisilamu - nzosavomerezeka kwa Mulungu, chifukwa ndi zipembedzo zopangidwa ndi anthu, kapena zipembedzo zomwe zidali zamulungu kenako nkusokonezedwa ndi manja a anthu, pomwe chisilamu ndi chipembedzo cha Mbuye wa Zolengedwa zonse, sichingasinthe kapena kusinthika, ndipo buku la chipembedzochi ndi Qur'an yopatulika, ndi buku losungidwa monga momwe Mulungu adalivumbulutsira ndipo likadali m'manja mwa Asilamu mpaka lero m'chinenero chomwe lidavumbulutsidwa nacho kwa Mtumiki womaliza.

Chimodzi mwa maziko a Chisilamu ndi kukhulupilira atumiki onse amene Mulungu anawatuma, onsewo adali anthu, Mulungu adawapatsa zisonyezo ndi zozizwitsa, ndipo adawatumiza kuti aitanire anthu kuti apembedze Iye yekha, popanda ophatikizana nawo. Womaliza mwa azithenga ake ndi M'thenga Muhammad (SAW) Mulungu adamutumiza ndi lamulo lomaliza lomwe limafafaniza malamulo a atumiki amene adalipo patsogolo pake, ndipo adamuthandiza ndi zizndikiro zazikulu ndipo chachikulu kwambiri ndi Qur'an yopatulika, liwu la Mbuye wa zolengedwa zonse, Buku lalikulu kwambiri lodziwika kwa anthu, lozizwitsa m'menemo, m'mawu ake, dongosolo lake, malamulo ake, ndipo m'menemo muli chiongoko cha kuchoonadi chobweretsa chisangalalo Padziko lino lapansi ndi tsiku lomaliza ndipo ndithu idavumbulutsidwa m'Chiarabu.

Pali maumboni ambiri omveka kuchokera mu nzeru ngakhale maphunziro omwe akutsimikizira popanda chikaiko kuti Qur'an iyi ndi mawu a Mlengi, Ulemerero ukhale kwa Iye, ndikuti sizingatheke kukhala zonena za anthu.

Zina mwa maziko a Chisilamu ndi kukhulupirira angelo ndi kukhulupirira tsiku lomaliza, pamene Mulungu adzaukitsa anthu m'manda

awo pa tsiku lachimaliziro kuti awawerengere pazochita zawo, choncho amene anachita zabwino ali wokhulupirira adzapeza chisangalalo chosatha ku m'Paradaiso, ndipo amene Akanira ndi kuchita zoipa, adzakhala ndi chilango chachikulu ku moto. ndipo mwa maziko a Chisilamu ndiko kukhulupilira zimene Mulungu adakonza nzabwino kapena zoipa.

Ndipo Chipembedzo cha Chisilamu ndi njira yokwanira ya umoyo, yogwirizana ndi Chilengedwe ndi nzeru, ndipo chimalandiridwa ndi mitima yangwiro, idakhazikitsidwa ndi Mlengi Wamkulu pa zolengedwa Zake, ndipo ndi chipembedzo cha ubwino ndi chisangalalo kwa anthu onse padziko lapansi ndi tsiku lomaliza, silisiyanitsa gulu la munthu wina ndi wina, ngakhalenso mtundu wina kuposa wina, ndipo anthu m'menemo ndiwofanana, palibe amene ali wopatulika mu Chisilamu kupatula ndi mulingo wa ntchito zake zolungama.

Mulungu wapamwamba adenena:

(مَنْ عَمِلَ صَٰلِحا مِّن ذَكَرٍ أَوْ أُنثَىٰ وَهُوَ مُؤْمِن فَلَنُحْيِيَنَّهُۥ حَيَوٰة طَيِّبَة وَلَنَجْزِيَنَّهُمْ أَجْرَهُم بِأَحْسَنِ مَا كَانُواْ يَعْمَلُونَ)

(amene akuchita zabwino, wamwamuna kapena wamkazi uku ali msilamu timkhazika ndi moyo wabwino (pano pa dziko, ndi tsiku la Kiyama) Tidzawalipira malipiro awo mochuluka kwambiri, Chifukwa cha zabwino zomwe ankachita.) [Al-Nahl: 97].

Zina mwa zimene Mulungu akutsimikiza m'Qur'an yopatulika ndi kuti kukhulupirira kuti Mulungu ndi Mbuye ndi wopembedzedwa, Chisilamu ndi chipembedzo, ndi kuti Muhammad ndi Mtumiki, ndi kulowa m'Chisilamu ndi chinthu chofunikira chomwe munthu alibe kuchitira mwina, Tsiku lachimaliziro padzakhala chiwerengero ndi malipiro. Amene ali Msilamu wokhulupirira woona, adzapambana ndi kupambana kwakukulu. Ndipo amene anali wokanira adzakhala ndi kuluza koonekera.

Mulungu wapamwamba adanena kuti:

(... وَمَن يُطِعِ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥ يُدْخِلْهُ جَنَّٰت تَجْرِي مِن تَحْتِهَا ٱلْأَنْهَٰرُ خَٰلِدِينَ فِيهَاۚ وَذَٰلِكَ ٱلْفَوْزُ ٱلْعَظِيمُ، وَمَن يَعْصِ ٱللَّهَ وَرَسُولَهُۥ وَيَتَعَدَّ حُدُودَهُۥ يُدْخِلْهُ نَارًا خَٰلِدا فِيهَا وَلَهُۥ عَذَاب مُّهِين)

(... Ndipo amene angamvere Mulungu ndi Mtumiki wake, adzamulowetsa m,minda yomwe pansi pake mitsinje ikuyenda. adzakhala m'menemo muyaya. kumeneko ndiko kupambana kwakukulu.

Koma amene anganyoze Mulungu ndi Mtumiki wake, ndi kulumpha malile ake, (Mulungu) adzamulowetsa kumoto; nadzakhala mmenemo muyaya. ndipo adzapeza chilango chosambula). [Al-Nisa:13-14].

Amene akufuna kulowa m’chisilamu anene kuti:(ddikuikira umboni kuti palibe wopembedzedwa mwachoonadi koma Mulungu m'modzi yekha ndipo ndikuikira umboni kuti Muhammad ndi M'thenga wa Mulungu),podziwa tanthauzo lake ndi kukhulupirira, ndipo m’menemo amakhala Msilamu. Kenako amaphunzira malamulo ena onse a chisilamu pang'onopang'ono. Kuti achite zimene Mulungu wamulamula.

kuti mumve zambiri: https://byenah.com/ny

الفهرس

CHISILAMU 3

Chipembedzo chogwirizana ndi chilengedwe, nzeru ndi chobweresa chisangalalo. 3

Ndani adakulenga iwe? 3

Kodi n'kutheka kuti Mulungu anatilenga n'kutisiya osasamala? Kodi zingakhale kuti Mulungu analenga zolengedwa zonsezi popanda chifukwa kapena cholinga? 5

Chifukwa tikudziwa kuti sitingadutse moyo uno popanda aliyense mwaife kulandira mphotho ya zomwe adachita, zabwino kapena zoyipa; ndiye sipadzakhala chilango kwa ochita zoipa, komanso malipiro abwino kwa ochita zabwino? 6